MULUNGU WOYAMBA MU ADVENTI – CAKA A 02 DECEMBER 2007

Mau Oyamba: Isaiya 2:1-5
Mau Achiwiri: Aroma 13:11-14
Mtenga Wabwino: Mateo 24:37-44

TIKHALE OKONZEKA POYEMBEKEZA KUDZA KWA AMBUYE

Nyengo ya Adventi imayamba chaka chachipembedzo chachikristu mu mpingo. Chaka chonse cimapenya pa tanthauzo ya cikhulupiliro cathu mwa Khristu. Ife m'Zambia timayamba takonzeka kulandira Ambuye Yesu pakati pathu ndi chilakolako chachikulu. Tili ndichilakolako cifukwa tidziwa momwe Yesu Kristu alili kwa ife. Iye ndiye mpulumutsi olonjezedwa ndi muomboli wa anthu onse ndi zolengedwa zonse zimene Mulungu anazilenga mwa iye kuyambila pachiyambi kuti anthu onse atengeko mbali mofikikapo mu umoyo ndi chikondi cha Mulungu. Koma umunthu wanthu omwe uli ndi malile, sungathe kufuna-funa cholinga chake chabwino ndi ku kana zoipa. Zimenezi zimatiletsa kutsata cikondi ndi ubwino wa Mulungu. Koma Mulungu salekeza kusamalira anthu ndi dziko zomwe analenga mu chikondi chake. Tonsefe tidziwa bwino kuti zimenezi ndi za zoona muno mwathu mu Zambia.

Mu nyengo ya adventi, timakondwerera pa kupempbeza ndi ciyembekezo cimene tifuna podikhila ufumu wa Ambuye Yesu Khristu pakati pathu mu moyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Kodi ufumu wa Mulungu ndi ciyani? Ufumu wa Mulungu ndi cilungamo, ubwino, ndi chikondi cha Mulungu comwe cifuna kugonjetsa kusowa chilungamo, choipa chilichonse, ndi kudana komwe kumaononga ndi kupha anthu ndi zinthu zonse zabwino. Kodi ndi chiyani comwe cititekesa muno mu Zambia kuti tikhale ndi chilakolako colandira ufumu wa Mulungu? Ndi cifukwa ca kuti tifuna choonadi, kuwara ndi mphamvu zakuti tipitirize kulimbika pa kukana zonyengo ndi kukananso zonse zomwe zimatipereka ku zotisocheletsa mu makhalidwe abwino a umunthu wa aliyense ndi wa mbumba yonse komanso zonse zopondeleza ndi nchito ya udani zomwe zimaipitsa ndi kuononga mtundu onse wa anthu.

Mprofeti Isaiya akunena kuti kwa ife "tiyeni tikwere ku phiri la Mulungu kuti akatiphunzitse njira zake, kuti tizidzitsata…tiyeni tiyende mkuwala kwa Mulungu". Paulo atiuza kuti "tiyeni tileke nchito za mu mdima, ndipo tinyamure zida zomenyera nkondo, tiyende moyenera monga anthu oyenda mkuwala" zida zimene Paulo alikulankulapo ndi zipangizo ndingagwilitse nchito kupeleka umoyo patsogolo. Ndiponso zinthu zimene zimapanga anthu kuti akhale ndi moyo wa ulemelerero. Isaiya walota chiyembekezo kuti anthu "adzasula malupanga awo kuti akhale makasu, ndiponso mikondo yao kuti ikhale mipeni". Chmachitika ngati tifunafuna kuti tileke kuzikonda ndi kuyamba kuchita zonse zimalenga kugawikana, mikangano ndiponso kusowa kwa kokondana**.** Ngakale munyumba mwatu, mumabungwe, amuna ndi azimayi ndiponso muchipembedzo, mu miyambo, mundale za ziko, mu chuma cha ziko latu la Zambia. Ni mtima wotani omwe uli kufunika tithane mukulimbikira? Paulo anena kuti "Yesu Khristu mwini akale zida zanu" zida za Yesu Khristu ndi mpamvu za mzimu wa mulungu, moyo wamene umaptsa chikondi ndi luntha. Mzimu unaza kupasa ife anthu zida, kuti tipunzire njira zake ndiku yenda mu njira yake.

Mulungu ali kupitirizabe kulankula ndi munthu aliyense ndi gulu lonse la anthu m'mtima ku pyolera mu zochitikha pa moyo wa anthu. Ndiponso kupyolera mu ubwino wazolengedwa pa ziko la pans. Ku onjezera amalankula nafe kupyolera mu mwana wake umodzi Yesu Khristu wamene anatengako mbali mu umunthu kuti atininkhe chikondi chake cho zipereka. Ndiye mwamene amatipatsira mpamvu za mzimu woyera, kuti tigonjeste mokwanira mpamvu zoipa ndiponso kufunisitsa kuchita zabwino mu moyo wathu onse. Zimachitika monga iye, ngati tapambana kuzikonda, ndi kukonda anzathu kupyolera muchisanzo chake. Kuzipereka mwa cikondi kwa abale athu [Yohane 13: 15]. Mbiri ya anthu a Mulungu ifunika kupitilira kukambirana cikondi cotiyanjanitsa ndiponso kubweretsa cilungamo ndi mtendere pa gulu la anthu ndi Mulungu mwa Yesu Khristu.

Yesaya aitana anthu onse a Mulungu kuyembekeza ndi kufunitsitsa kubwera kwa Mulumutsi wolonjezedwa uja. Pa nyengo ya Adventi, timakonzekera kusangalala kwa nthawi yambiri pamene Mpulumutsi anabadwa koma kuti akhale Mulungu yemwe ali nafe, Emmanueli, munthu ngati ife tomwe. Anabwera kuti ufumu wa Mulungu ukhale pakati pathu, mwa iye kupyolera m'kulalika uthenga

wabwino, uthenga wa cipulumutso, mu mau komanso macitidwe. Cifukwa ca iye, anamkana, komanso anaphedwa. Koma Yesu anapambana zakwaipa ndi infa, zosalungama ndi zopsyinja, pouka kwa akufa cifukwa ca ife. Pakutero, anatiphunzitsa kuti ifenso tizicita cimodzi-modzi. N'cifukwa cake, ife akhristu mu Zambia, tingalimbane ndi bvuto la ziphuphu, pofuna kuti omwe ali pa nchito alandire malipiro abwino, kufanana kwa amuna ndi akazi pa zacitukuko, napanga umphawi nkhani ya kale.

Mu uthenga, Ambuye akutiphunzitsa nyengo yomwe mbiri yathu komanso ya dziko lathu lizatha. Akutilimbitsanso kuti tipitilize kupenya komanso kupilira kuti tigonjetse mabvuto omwe mwa ife, ndi mu dziko lathu omwe, mwabodza zimatiletsa kuthandiza anzathu pa nchito za mtendere ndi cilungamo, kucilitsa ndi kuyanjana, pofuna-funa ubwino wa onse. "ukwali nsoke, takwafwile muntu." Kuthanthauza kuti pali ubwino waukulu kumvera cenjezo yocokera kwa ena. Koma timangozifunira zabwino mnalo mwa anzathu, pakuwapondeleza, ndi kuwalanda umuthu wao.

M'nnyengo ino ya Adventi, ife muno mu Zambia tifunika kudzifunsa pa mkhalidwe wathu ndi anthu ena, m'mabanja athu, mzimbumba zathu, anthu omwe tiyandikana nawo, mnchito zathu, ndi zosankha za umuntu wathu. Tifunika kupemphera kuti tikwanitse kutengako mbali mokwana mnchitoyi momwe tingathe kuchilitsidwa ndi Ambuye Yesu m'makhalidwe oipa, conco tingathe kumlandira ndi chimwemwe iye amene anatibadwira kuti tikhale naye mu ufumu wake wa chilungamo ndi mtendere kuyambira tsopano. M'mawu a katswiri wa masalimo, titha kuyamba mwa tsopano kunena kuuza wina ndi mzace moona kuti " Mtendere ukhale nanu" ngati tayamba kuuzana moona kuti " nifunafuna kuti mukhale bwino!"

MAFUNSO OSINKHA-SINKHA KOMANSO KUGAWANA MU MAMBUMBA

- Kodi ufumu wa Khristu uli motani, ndipo cifukwa n'ciani tiyenera kulaka-laka kuulandila muno mu Zambia?
- Kodi tibvale zotani kuti tipambane nkhondo ya macimo yosowetsa cilungamo pakati pathu?
- Kodi Yesu atithandiza motani kuti tipambane zomwe zimatilepheretsa kuzetsa mtendere ndi cilungamo pa za ndale, citukuko, komanso miyambo mu Zambia?

SEWERO

Pakhale anthu anai. Umodzi azizunza anzake. Wina abwere kudzaombola anzake ku unyolo wopsyinjidwa ndi kupondelezedwa atamva kulira kwao. Pothera pake, anthu onse a mbumba yonse akhale okondwela cifukwa comasulidwa mokondwela.

MAPEMHERO A AKHRISTU

- Tipempha, Ambuye, kuti mutitumizire mzimu wa cikondi komansonzeru kuti pa umunthu ndi mbumba yathu tiyende m'njira ya mtendere ndi cilungamo. Ambuyemutimvere. Tikupemhani, mutibvomereze.
- Tipempha, Ambuye, kuti mutitsekule maso athu kuti tione phindu lolandira ufumu wanu womwe udzatiombola ku ukapolo wa macimo. Ambuye, mutimvere. Tikupemphani, mutibvomereze.
- Tipempha, Ambuye, kuti mutithandize kufunira anzathu zabwino pogwira nchito za cilungamo ndi mtendere mu mambumba athu mu Zambia. Ambuye, mutimvere. Tikupemhpani, mutibvomereze.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E-mail: jctr@jesuits.org.zm Website: www.jctr.org.zm

LA MLUNGU LA 2 MU ADVENTI – CAKA CA A 09 DECEMBER 2007

Cowerenga Coyamba: Isaiah 11:1-10
Cowerenga Caciwiri: Aroma 15:4-9
Mthenga: Mateyo 3:1-12

TILAPE NDI KUBEREKA ZIPATSO ZABWINO KUTI TILANDIRE YESU KHRISTU MPULUMUTSI WATHU

Pemphelo lotsegulira lero itipempha kucotsa zinthu zimene zitiletsa kulandira Khristu mwamtendere. Ndiyo pempho imene Yohane Mbatizi apanga kwa ife amene mwa njira yapadera, takhala tikusintha ndipo tikalikusinthabe miyoyo yathu, mabanja athu ndiponso madera athu kuti zikhale cipululu ceni-ceni. Tingadzifunse mafunso awiri awa: yoyamba, kodi Khristu akubwelera ciyani? Yaciwiri, Kodi ndi zinthu zotani mu umoyo wathu ndipo m'madera athu zimene tifunika kucotsa ngati tifunadi kulandira Khristu. Yankho ku funso loyamba ndi iyi: amabwera kotero kuti ndi mkhalidwe wake wa nzeru, agalimbitse nzeru zathu kotero kuti tikwaniritse kunvetsa ndi kuwona bwino ma ubale athu mwa coona ndi cilungamo. Abwera kweni-kweni kuti atiitane ndi kutipatsa mphanvu zoti tipitilize kugwira nchito ndi kulimbikira pamodzi naye kotero kuti tingapange cipululu ca miyoyo yathu ndi madera yathu, umunthu wathu ndi zotizungulira kuti ziyambe tsopano lino kukhala za maluwa. Ndipo tikatsiliza ulendo wathu wa padziko, miyoyo yathu yonse yatsopano indzaunganitsidwa pamodzi mu ulemelero wake, mu umoyo weni-weni ndi iye, pamene atilandra mu ufumu wake. "mwana wanchete olilira pansi" (mwana wansiwa sadzakhala akudandaula kapena kulira koma adzanyamuka ndi kukalima padothi).

Umo ndimo m'mene ziliri tsopano, inde, tsopano lino. Ino ndiye nthawi imene ife anthu a mu Zambia tifunika kubzala mbeu za cilungamo ndi mtendere m'mabanja athu, mzimbumba zathu ndi mdziko lathu, kotero kuti tikwanilitse kubereka zipatso mwa unyinji, zipatso zabwino zimene ufumu wa Yesu, ufumu wacoona umafuna. Kodi ndicifukwa ciyani atipempha kubeleka zipatso zabwino? Cifukwa iye ndiye amene amatipatsa moyo ndiponso amatipatsa mbeu yabwino imene imafunika kotero kuti moyo wathu ndiponso moyo wadziko lonse lapansi ungapitedi patsogolo. Izi zingacitike ngati palibe njala ndi ludzu ndipo ngati palibe aliyense amene akukhala wolemetsedwa, koma ngati aliyense akukhala wodzadzidwa ndi zinthu zabwinodi ndipo akhala wosangalala monga m'mene amai athu Maria, amai a Ambuye athu Yesu Khristu anasangalalira mu nyimbo yawo ya matamando pamene mbeu ya mwana wa Mulungu inabzalidwa mwa iwo panthawi yolengeza za kubadwa kwa Yesu (Luka 1:46-65). Tsopano tingayambe kusangalalira mbeu za cilungamo ndi mtendere, cikhulupiliro ndi kuyanjana cifundo ndi cikondi, zimene Mulungu amabzala munthaka yabwino ya umoyo wathu, ndipo ife timazithilira ndi citungu ca kulimbikira kwathu. Mphatso yake yoyenera ndi citsanzo coona ca kuyembekeza kwathu, pamene zonse zidzakhala za tsopano mwa Yesu Khristu kwa muyaya ndipo nchito zathu zabwino zidzakoloredwa.

Tsopano tingabwere ku funso yathu yaciwiri: ndi zinthu zotani zimene tiyenera kucotsa ngati tifuna kulandira Khristu pakati pathu? Nagti tifuna kukwanilitsa colinga ca Khristu pa ife, tifunika kucotsa zinthu zimene zimafuma mu nzeru za munthu cabe, ndipo zimatayana ndi colinga ceni-ceni ndi ulemelero umene Mulungu analinga potilenga. Tifunika kupewa kugwiritsa nchito mau monga, "iwe na ine sitidzakambitsana mpaka kumanda". Mwacidule, kawiri kawiri timalephera kufikapo pa umunthu wathu weni-weni cifukwa nzeru za umunthu wathu pazokha ndizapafupi ndipo ndi zopelewera. Angakhale kuti zikome bwanji, tifunikabe mzimu wa Khristu kuti, paciyambi pa zonse, tingazindikire zonse zimene zikubweza pansi ulemelero woona wa umoyo wathu ndiponso mkhalidwe wathu ndi anzathu.

Indedi, tidzakwanilitsa kupeza njira zimene tifunika kuti tiyambe kusintha zicitidwe zoipa zimene zakhala zikutipweteka ife komanso anzathu. Tiyenera kuzisintha kuti zikhale zinthu zabwino kwa onse, zokomera onse. Kodi izi zingatheke bwanji? Yesaya atipatsa yankho pomwe afotokoza za Mesiya mnjira yotere: "Pa iye mzimu wa Mulungu ukhala, Mzimu wa nzeru ndi wa kudziwitsa, mzimu wopeputsa ndi wamphamvu, mzimu wakudziwa ndi kuopa Mulungu." Yesu Khristu yemwe ali liu ndi

nzeru za Mulungu, anakhala munthu ndi kukhala pakati pathu kuti potenga umunthu wathu kwa iye angatipange kukhala oyonera kugawana naye mu nzeru zake zimene zitionetsa njira ndipo zitipatsa mphamvu zokhalira anthu a ulemerero mwa iye ndipo kudzera mwa iye.

Kodi tingazindikire bwanji coona ca maganizo athu, maonedwe athu ndi kusankha kwathu pa zinthu zokhuza umoyo wathu ndi anthu ena, m'mabanja athu ndi mzimbumba zathu? Tingazindikire bwino ngati tiri okonzeka kusiyanitsa ngati zicokera ku mzimu wa khristu kapena mzimu woipa. Kodi tingadziwe bwanji kuti tikutsogoleredwa ndi mzimu wa Yesu Khristu? Ndipokhapo tikayamba kuganiza ndi kucita zinthu nagti Yesu Khristu iye yewme, ndipomwe tingafune zinthu zabwino kwa ife ndi anthu ena onse. Maka-maka tifunika kuika nzeru pa anthu omwe moyo wao suli bwino, iwo amene abvutika cifukwa cha umunthu wao, iwo amene alibe cakudya pomwe kuli zinthu zambiri zabwino kwa onse mu Zambia, iwo amene akali ana koma alibe maphunziro abwino ndi maluso omwe angawathandize kupeza nchito, ndi zina zotere.

Tiyeni tipenye mokhulupirika pa zinthu zomwe zakhala zikucitika mu Zambia posachedwapa. Tifunika kudziwa bwino momwe muzimu woipa umatikopa ife: timakhala anthu odzikonda ndi ozifunila zabwino mu njila iliyonse, pakudzikudza ndi pakupondeleza ena ndiponso pakuzifunila mpata wabwino wobweretsa ciphuphu pakati pathu. Ndipokhapo tikakhala okonzeka kulandila ena monga momwe Mulungu afunila kuti tizicitira ngati ana a banja limodzi, kuti tizikhala okonzeka kulandira Yesu pakati pathu, mu umoyo wathu ndi komwe tikhala. Ndi nthawi yomweyi pomwe timayamba kukhala ngati anthu a mtendere ndi ufulu monga momwe mprofeti Yesaya ationetsa mu cithunzi comwe atipatsa cociritsa mipatuko yonse ndi zonse zomwe zimaononga mkhalidwe komwe tikhala ndi ponse-ponse. Ndife oitanidwa kuweluza mwacilungamo ndi molinganiza momwe Mulungu amacitira ndi kutionetsa ndiponso amatipatsa mphamvu kucita cimodzi-modzi.

Ndicifukwa cake Paulo woyera atiuza kuti tisataye ciyembekezo ndi kuleka kuyesa kupanga umoyo wathu ndi wa anthu onse wa umunthu ndi wa umulungu mopambana. Zimenezi tinalonjezedwa ndipo tidzapatsidwa. Cifukwa? Motani? Cifukwa Mulungu ali pafupi ndi ife ndipo ndi okonzeka kutithandiza nthawi zonse. Mulungu amatithandiza munjira zitatu maka-maka: coyamba pakutsata citsanzo cake ndikukhala omvetsana. Caciwiri ndiponso cabwino kuti monga iye tiyambe kucita zinthu ndi ena mokhululukirana ndi mwaubale osati ngati adani. Cacitatu ndiponso comwe cili cofunika kwa ife ndikuti ndi iye ndipo ngati iye tikhale odzicepetsa ndi kukhala otumikilana monga momwe anationetsera pakusambitsa mapazi a ophunzira ake, utumiki omwe upanga anthu kukhala okonzeka ngakhale kudziiwala cifukwa ca ena. Pa zonse, ndi zomwe Yesu Khristu anacita.

Mu uthenga wa lero, Mateyo atiuza kuti mu ubatizo, coyamba timabatizika ndi madzi omwe amatitsuka zoipa zomwe ticitira ena, ubatizo omwe umatitsekulira kuli Yesu ndi ena. Ubatizo wa madzi utipeleka ku ubatizo mu moto ndi mzimu, ubatizo omwe Yesu Khristu mwini anaulandira pa mtanda pomwe anamwalira ndi kuuka kwa akufa cifukwa ca ife ngakhale tikali ocimwa. Uyu ndi ubatizo wa pa mwamba, ubatizo omwe utipatsa mphamvu mwa mphatso za mzimu wa Yesu, kupitiliza kuyesetsa, kuyenda mnjira zake mwa kuti pomwe zonse zikapangindwe kwa tsopano, tikalamulire ndi iye mu ulemu mu ufumu wake wa mtendere ndi cikondi, cilungamo ndi kuyera. Amen.

MAFUNSO OSINKHA-SINKHA NDI KUGAWANA MU MA MBUMBA

- Kodi ndiciyani comwe cingatithandize ngati anthu mu ma mbumba athu kupeza coona mumaganizo athu ndi zinthu zomwe timasankhula mu umoyo wathu ndi wa ena?
- Kodi ndi ciyani comwe cimatisunga kuti tisataye ciyembekezo mu umoyo wathu pa ife tokha komanso ngati mbumba?
- Kodi ndi njira zotani zomwe mphamvu ya ubatizo imaonetsa mu umoyo wanthu wa tsiku ndi tsiku.

SEWERO

Pakhale munthu umodzi yemwe ali ndi moyo wobvuta, cidakwa ndiponso munthu osasamala zinthu za ena. Tsiku lina iye akumana ndi mkhirstu weni-weni yemwe amthandiza munthuyo kuzindikira kufunika kwa kusamalirana mu umoyo wathu. Munthuyo asintha ndi kupita kwao pakucita zazikulu pakubweretsa ubwino.

MAPEMPHERO A KHRISTU

- Tipempherere mzimu wofuna kupeza coona kuti tizisankhula zinthu zoyenera mu umoyo wathu ngati anthu komanso pa mbumba. Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutibvomereze.
- Tipemphere kuti tikhale olimbika ndi kusataya ciyembekezo ngakhale tikumane ndi mabvuto. Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutibvomereze.
- Tipempherere citsogolero ca Mulungu kuti tikwanilitse malonjezo omwe tinalonjeza pa ubatizo. Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutibvomereze.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E-mail: jctr@jesuits.org.zm Website: www.jctr.org.zm

LA MULUNGU LA 3 LA ADVENTI CHAKA A 16 DECEMBER 2007

MAU OYAMBA: YESAYA 35: 1-6, 10.
MAU ACHIWIRI: YAKOBE 5: 7-10.
UTHENGA WABWINO: MATEYO 11: 2-11.

MUSATAYE MTIMA, MPULUMUTSI WATHU AKUBWERA

Pa nyengo ino ya Adventi, Mpingo ukutipempha tonsefe kupemphera kuti tikachite chikondwelero cha kubwera kwa Yesu Kristu, Mpulumutsi wathu, ndi cikondi ndi mathokozo poyandikira caka ca Khrismasi. Kodi zimenezi zingatheke bwanji kwa ife pokhala nzika za Zambia? Pokhapo ngati tisinkhasinkha pa izi: kodi Yesu Khristu atipulumutsa ku ciyani popanda kusinkha-sinkha pa izi:- Kodi Yesu Khristu atipulumutsa ku ciani? Komanso ndi pacifukwa cotani? Yankho ya pafupi ndi yakuti Yesu Khristu anabwera kudzatimasula ku unyolo ndi ciwonongeko kuti tikhale aufulu, otha kumanga ndi kusangalatsa miyoyo yathu. Kodi sicimeneci cimene ife timazifunira tokha, komanso ana athu ndi abale athu? Pomwe Mose anakhazikitsa phangano la Mulungu pa anthu ake, anawapempha zimenezi, kuti mwina abvomere kapena kukana, komanso kuti mwina asankhule moyo kapena imfa (Deut. 30:19) Kobvomera phangano la mulungu, kukana tanthauzo lake, kusankhula kuika ciyembekezo ndi cikhulupiriro cao conse mwa Mulungu yemwe ali kasupe wa moyo ndinso wokometsa moyo wao, komanso gwero la moyo wathu, kukana phangano, nuika cikhulupiriro ndi ciyembekezo mwa iwo okha osati mwa Mulungu kapena mwa cidule, kusakhala ndi ciyembekezo ciri conse mu umoyo? Motero, umoyo umakhala ngati wakalabvula gaga ndiponso umayesedwa ngati nthaka yopanda pace, pamene sipangapezeke moyo uli wonse. Tsopano ndi zotani zimene ifeyo tikusankhula? Ndikhulupirira kuti tingayankhe m'mene ana a Israele anacitira pamene onse anafuula ndi liu limodzi kuti anafuna kuika cikhulupiriro cao mu phangano la Mulungu. Koma, kodi yankho yotere imacokeradi mu mitima yathu ndi m'mganizo athu, kapena mu mau athu cabe? Ngati tifunitsitsadi kutanthauza zomwe timalankhula, tifunika kuzifunsa mafunso mafunso awiri:- Coyambirira, kodi tizindikira ndi kulawako zimene tingapulutsidweko mu umoyo wathu pa ife tokha, komanso ngati mabanja, ngati mbumba za Cikhristu, ngatinso dziko la Zambia? Ndipo ca ciwiri cake, kodi tizindikira ndinso kulawako zocitika za miyoyo yathu, kuti ciyembekezo ndi cikhulupiriro, ndinso cikondi ndi mathokozo zimene zimabwera pa kubvomera ndi kutsatira Ambuye Yesu, cipangano ca tsopano, cimene cimatilimbitsa nthawi zonse ndi kutipatsa mphamvu zosandulitsa cipululu ca moyo wathu kuti ciphukire?

Tsono, tiyankha funso loyamba: Kodi ndikuciyani komwe tiri kufuna kuti Ambuye Yesu atipulumutse? Poyamba tiyeni tione m'mene zinthu ziliri mu dziko lathu lino la Zambia, ndipo titacita zimenezi tiyambe kupeza yankho ya funso lathu - kodi ndikuciyani komwe Yesu Khristu akufuna kutipulumutsa? Polengeza za kubwera kwa Mpulumutsi wotiombola, mporofeti Yesaya analozera zimene Yesu Khristu ankayenera kuzisonyeza kwa ophunzira a Yohane Mbatizi omwe iye anawatuma kwa Yesu kukamufunsa kuti: kodi ndiye amene tinkayembekeza kapena tiyembekezere wina wace? Yesaya akutisangalatsa potiuza kuti tisataye mtima koma kulimbitsa manja athu olema, kulimbitsanso maondo athu, ndinso kukhala olimba, komanso kukhala ndi khumbo la tsopano mu umoyo. "Dzedzere-dzezere salingana nugweratu" Zotitaitsa mtima kapena zowawa zitha kukhalapo, koma ndicaulere ca Mulungu titha kupambana. Koma ngakhale ziri tero, Mulungu afuna poyamba kuti tionepo pa umoyo wathu wa mabvuto, munthaka ija yoipa m'mene titha kudzibweretsa ife tokha ndinso anzathu ndizilakolako zathu zonyansa, maganizo ndi zicitidwe zathu ndinso kulephera kucita zabwino. Tifunika kuzindikira zinthuzo, komanso makhalidwe ndi zofunika pa umoyo wathu zomwe zimaipitsa mitima yathu, ndinso cibale mbanja kapenanso pakati pa abwenzi ndi abale pa mbumba, pa sukulu, pa nchito, pa malonda, pa ndale mdera lathu, kapena mdziko lonse. Ndi cifukwa cake timafuula ndi yemwe analemba mu Salimo: Kodi thandizo langa limacokera kuti? (Masalimo 120:1). Tingayambe kufuna njira yotitulutsa mdzenje lomwe takhala tiludzikumbira ife tokha komanso kukumbira ena. Tingayambe kufuna njira zolimbitsiramo cibale cathu. Koma mwamsanga-msanga titha kunena ife tokha kuti tayesa kwambiri koma ndiye zonse nzopanda pace. Ndipo yankho mmitima yathu yazilala. "Thandizo langa licokera kwa Mulungu amene analenga dziko la kumwamba ndi dziko la pansi pano!" Ncifukwa cake uthenga wa mneneri Yesaya utiuza kuti Mpulumutsi wa Mulungu, Yesu Khristu, ndiye amene azabwera kudzatipatsa ciyembekezo ceni-ceni, cotipatsa mphamvu ndi kupambana kuti tituluke mu zonyansa m'mene taziika ife tokha ndi anzathu nthawi yonseyi. Amatithandiza kuyangana pa zizindikiro zomwe zitisonyeza m'mene Mulungu ndi Mpulumutsi wathu Yesu Khritu salephera kutithandiza ndinso zomwe atha kuticitira iwo amene aika cikhulupiriro mwa iye, amene alibe cikaiko ciri conse kuti azasunga lonjezo lotipulumutsa. Mwa ici, tidzakhala ndi cifukwa ceni-ceni cokokera mphamvu zathu zonse pamodzi ndikuyamba kuyenda monyadira ndipo pa mbuyo pake kuyamba kulimbitsa ndi kuthaniza ena kucita cimodzi-modzi maka-maka iwo ali pafupi nase, m'mabanja, m'madera athu, ndinso m'mbumba zathu za Chikhristu.

Tiyeni tsopano tiyambe tapenya pa zizindikiro zomwe zingathe kuticiritsa ife. Mulungu amatitsekula makutu pa nthawi zonse pamene tikhala agonthi ku zifuniro za anzathu, ndi ku zonse zimene amatiuza. Ndipo

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E-mail: jctr@jesuits.org.zm Website: www.jctr.org.zm

amatithandiza kuwamvera ndi kuwamvetsa. Amatitseklra maso pamene tilephera kupenya coona ca njira yoononga imene takhala tilukhalira ife tokha, ndinso mu umoyo wokhuza anzathu ena. Tsono amatithandiza kuyenda mwa ufulu mnjira yake yamtendere ndi cilungamo kuti ife ndi dziko lathu la Zambia tileke kunyalanyaza kugwebana ndi bvuto la umphawi ndi kubweletsa kulinganiza ndi cilungamo pa citukuko ca onse. Iye amamasula malilime yathu pamene atigwiritsa nchito kuti tisalankhule coona pamene tiona ciphuphu pamalo otizungulira. Umu ndi m'mene amatigamulira ndipo kutithandiza kunyamula ena amene ali olemedwa, maka-maka azimai amene amabvutitsidwa mu mabanja athu ndi mbali zina za umoyo mu madera athu, monga ku za maphunziro, citetezo ca umoyo ndinso kagwiridwe ka nchito. Ndiponso amasinthanso mkhalidwe wathu ku anthu acilendo, monga wothawa nkhondo ndinso wokanidwa mu madera athu, monga anthu odwala matenda a 'AIDS' ndipo tiyamba kuteteza ndi kuwalankhulira pa zosowa zao. Potsiliza, atiphunzitsa ndi kutithandiza ife osati cabe m'mene tingathe kusamalira mwa cikondi ana a masiye ndi akazi ofedwa, ndinso iwo amene ali ndi kalombo ka "HIV ndi AIDS" komanso kusintha khalidwe la banja lathu ndi mkhalidwe wokhuza ena umene utha kuwanditsa matenda otengera a “HIV ndi AIDS”. Izi ndizo zizindikiro za nchito za zing'ono ndi zazikulu zomwe Ambuye Yesu amapereka mphamvu kwa iwo amene aika cikhulupiriro cao"mwa iye" kuti azidzicita. Ndipokhapo pamene tayamba kucita mcoonadi ndinso nthawi zonse zizindikirozo pamene tilowa mbiri yokhazikitsa ufumu wa Mulungu. Njira imeneyo yayamba kale kuzika mizyu ndinso kubereka zipatso mwa ife ndi pakati pathu muno mu Zambia. Kodi tizasankhula ciyani pamene tiona zizindikiro zopatsa moyo zomwe caulere ca Yesu Khristu zitha kucita ndinso zomwe caulere cimineci cilucita pakati pathu? Kodi tizamulandira Yesu Khristu ndi kukhala ophunzira ake ndinso kupitiriza kugwira naye nchito mokondwa pocita zizindikiro zimenezo? Ambuye Yesu amatiuza kuti popanda iwo, sitingathe kucita kanthu kali konse, koma ndi cithandizo cao titha kuzula mapiri akulu a mpsinjo ndi kupondereza. Aya ndi mapiri omwe timaika pa anzathu komanso omwe timanyamula ife tomwe amene aopsyeza umoyo wathu ndinso umoyo wa m'dziko momwe tikhala kuonjezeraponso kukoma ndikukongola kwa malo acilengedwe.

Tsono funso ndilakuti, kodi tingayende bwanji pa njira yakagwiridwe ka nchito kotipulumutsa pogwira nchito ya ufumu wa Yesu Khristu ya cilungamo ndi mtendere? Mwina mwace tingacite mantha pamene tikumana ndi nchitoyi yomwe iwoneka yopanda ciyembekezo ndiponso yobvuta. Mu kalata yathu ya lero, Yakobe Woyera atisonyeza m'mene tingacitire cimeneci kuti tisacite mantha, komanso kucita zinthu mwamsanga, kenaka nkulephera kapena kutaya mtima. Coyambirira tiyenera kuziphunzitsa kukhala anthu oleza mtima ndinso kusataya mtima pamene tikumana ndi zobvuta zirizonse, zazing'ono kapena zazikulu. Nthawi zina kucedwa kwa zinthu kumatitaitsa mtima pamene zinthu siziri m'mene tifuna zikhalire kapenanso pamene sitiona zipatso zathukuta lathu. Koma pamene tiphunzira kukhala oleza mtima, tiphunziranso kuyembekeza mwacangu, osati mozilala kubwera kwa citukuko mwapang'ono-pang'no koma mwa nthawi zonse, ndipo zotuluka zake za maganizo akukonza ndinso misintho yomwe takhala tilikugwirira nchito molimbikira mu madera athu ndi dziko lathu lino la Zambia. Kuleza kumeneku kufunika kwambiri pakati pa nzika za Zambia pofuna kukhazikitsa lamulo la tsopano lokomera anthu onse! Mkupita kwa nthawi tizaonadi kufunikira kwake kothetsa mikangano iliyonse, ngakhale mikangano ya zokhumba zathu, mbumba zathu za Chikhristu zomwe, zotilepheretsa kupititsa moyo wathu pa tsogolo. Kodi tingathetse bwanji mikangano yathu yotere ndi kuyanjana? Coyambirira ndi kupenyana ndi maso aulemu ngati abwenzi osati anthu okangana. Mnjira yotere titha pamodzi mcoona ndi mcikondi kugonjetsa zomwe zimatikanganitsa ndi kutilepheretsa kufuna ubwino wa onse. Ndikukhala acangu poleza mtima, ndinso kuyembekeza mwacangu, ndipo pamene tingakwanilitse kusataya mtima pa njira yaitali ndinso yonzunza, yobweretsa mtendere ndi cilungamo. Koma ndiye tileke mantha ndi kulimba mtima, ngati sititaya cikhulupiriro cathu mwa Yesu yemwe anapabana mphamvu za mdima ndiponso apitiliza kutiunikira pa ulendo komanso kupepusa zotilemera. Inde, umu ndimo tizakhalira woleza mtima ndikuyamba kucepetsa cisoni ndi madandaulo, ziphuphu ndi kuponderezedwa. Iye ndiye njira yokhayo yomwe tingayambireko kusekerera kubwera kwa okondeka, Mpulumutsi wathu Yesu Khristu ndi cikondi ndi mathokozo, ndi cimwemwe ceni-ceni ndinso ciyamik

MAFUNSO YOSINKHA-SINKHAPO POGAWANA M'MBUMBA

- Kodi ndi ciani comwe tingapeze cotizungulira comwe Yesu Khristu angatipulumutseko ndipo afuna kutipulumutsa cifukwa ca ciani?
- Mose anafunsa anthu kusankha pakati pa moyo ndi imfa. Kodi ndi zitsanzo zotani mu mabanja athu, m'mbumba za Cikhristu, dziko lathu, zomwe zisonyezadi kuti tikusankhadi moyo?
- Kodi ufumu wa Yesu Khristu uli ndi uthenga uliwonse wapadera mu za ndale masiku ano mu dziko lathu la Zambia?

SEWERO: Pakhale munthu m'modzi woyeserera wopempha amene ali kunyamula katundu wolema ndipo wopita ndi njira aimilira, ndikumsambitsa ndinso kumudyetsa. Wopemphayu tsopano apita uku ndi uku mwa cimwemwe ndi cisangalaro.

MAPEMPHERO A MBUMBA

- Tipemphe, Ambuye, kuti atiphunzitse kudziwa zomwe anabwera kuzatiphunzitsa kuti tiphunzitsenso ena kudziwa cipulumutso ceni-ceni. Ambuye mutimvere! Tikupenphani mutibvomereze!!
- Tipemphe, Ambuye, kuti atsogolere mbumba zathu kuti tizipanga maganizo opatsa moyo. Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutibvomereze.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E-mail: jctr@jesuits.org.zm Website: www.jctr.org.zm

LA MULUNGU LA 4 LA ADVENTI CHAKA A 23 DECEMBER 2007

Chowerenga Choyamba: Yesaya 7:10-14
Chowerenga Chachiwiri: Aroma 1:1-7
Uthenga, Mateyo: 1:18-25

MUSAOPE, MULUNGU ALI NAFE

Pa masabata ochepa apitawa, kumayambiliro a nyengo ya Adventi, mau a Mulungu anatichangamula, natidzutsa kuti tikhale ozindikira kufunikira kokhala anthu omasuka ku zinthu zomwe zitisowetsa mtendere mu umoyo wathu muno m'dziko la Zambia masiku ano. Motero tifunika kukhala okonzeka kulandira Yesu Khristu amene akubwera kudzatipulumutsa. Sabata lino lothera la nyengo ya Adventi lititthandiza kuona pa zomwe tifunika kuchita pomwe tachangamuka. Tifunika kusinkha-sinkha ndi kuona m'mitima mwathu komanso pa malo otizungulira kuti pomwe tiyesetsa kukonzekera kubwera kwa Mpulumutsi, tikhale ozindikira komanso otembenuka mtima ku machitidwe athu osalemekeza ulemelero wa umoyo wathu komanso umoyo wa anzathu. Popeza makhalidwe ndi machitidwe amenewa ndiwo amaononga ndi kuthetsa chibwenzi pakati pa ife ndi anzathu komanso pakati pa ife ndi Mulungu. Tsono tikayamba tero kutembenuka mitima ndi kumalapa, timaona kufunikira kwake kwa Yesu Khristu mu umoyo wathu kuti atichize mkubvulazidwa kwathu komanso kubvulazidwa kwa anthu onse m'dziko lathu. Apa ndi pomwe timayamba kuzindikira kuti tsopano tili kulandila Mpulumutsi amene akubwera nadzetsa chimwemwe ndi chiyembekezo kuti ndi zoona tsopano zinthu zidzayenda bwino komanso mchilungamo. Ngakhale zili chonco, kuti timayesako kusintha zinthu kuti umoyo wathu utiyendere bwino, nthawi zambiri timachita ulesi ndipo timafuna kuleka kuchitapo kanthu kalikonse kusintha umoyo wathu chifukwa sipaoneka kusintha ai. Sitiona phindu yake ya kuyesa kwathu, kotero kuti timakhala pafupi kungoleka ndi kumangokhala chabe.

Apa ndi pomwe timayamba kutaya chikhulupiliro chakuti titha kupeza ndi kuona umoyo wabwino, kapenso kuti umoyo wabwinowo titaupeza titha kukhala okondwera nthawi yaitali. Nthawiyi, timapereka zitsanzo komanso mafunso kwa Mipingo, Boma komanso atsogoleri ena onse. Timafunsa zomwe alikuchitapo pofuna kutithandiza ife klomanso dziko lonse lathunthu kupeza chilunganmo ndi mtendere makamaka kukhala dziko momwe ufulu wa anthu wachibadwidwe ulemekezeka komanso kutumphutsidwa. Chifukwa ndi chakuti, zomwe tiona nthawi zonse m'malo omwe tikhala ndi otizungulira ndi ziphuphu, kulimbirana utsogoleri kapena ulamuliro, kugwililira ndi kugona ana ndi azimai mwachipongwe, ndi mabvuto ena otero amene saoneka kutha kwake mwamsanga. Tsono timayamba kutaya chiyembekezo, ndipo kwa ife nthawi yotere chipembedzo chathu chimakhala chabe ngati njira motisangulutsira osati chinthu cheni-cheni chomwe chingatichotsere mabvuto athuwa ndi kusintha umoyo wathu. Ndi pa nthawi zotere pamene mau a Mulungu tsiku la lero afuna kutipempha kuti tione pa zinthuzi zimene zimachitika mu umoyo wathu. Mau a Mulungu lero afuna kuti tidzifunse kuti kodi tili ndi chikhulupiliro kapena ai. Ngati tili naco chikhulupiliro, ndi chikhulupiliro chotano chimene tilinacho? Pa nthawi zomwe zinthu zochitika mu umoyo wathu ziwopseza chikhulupiliro chathu, mau a Mulungu atiuza kuti titha kuchita zinthu ziwiri: kukhala ndi kusunga chukhulupiliro chathu kapena kukhala opanda chikhulupiliro, kumkhulupilira Mulungu kapena kukana kumkhulupilira, kukhala ndi chiyembekezo kapena kukhala opanda chiyemebekezo. Kodi kuteroko sikuchita monga Mfumu Ahazi anachitira, monga tamva m'mau oyamba ochokera m'buku la mneneri Yesaya? Kodi sitiyenera kuchita monga anachitira Yosefe, monga tamvanso mu Uthenga wa Mateyo?

Poyamba tiyeni tione za Mfumu Ahazi, mfumu yopanda chikhulupiliro imene inaiwala mbiri ya wanthu wa Israeli. Mbiri ya ana a Israeli ndi mbiri momwe tikumva za momwe Mulungu anakhulupilirika posunga pangano ndi lonjezo lake losamalira anthu ake a Israeli. Tsono mbiri imeneyi tikumva za m'mene Mulungu anakhalira nao pafupi ana a Israeli pomwe anakumana ndi mabvuto osiyana-siyana ndi pomwe pfuko lao la Israeli linaopsezedwa ku nkhondo, imfa, ndi matenda kapena miliri. Ndipo mbiri imeneyi ndiyo inali chikhulupiliro cha ana a Israeli chomwe amafunika kuchula pa kupemphera tsiku ndi tsiku la umoyo wao. Koma m'malo modalira mphamvu, chitetezo ndi thandizo ya Mulungu, Mfumu Ahazi anadalira mphamvu za gulu lake la nkhondo limene mphamvu zake zinali zochepa. Mfumu ahazi anadaliranso thandizo ndi mgwirizano wa Mfumu ya dziko lina imene anali yosadalirika.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E-mail: jctr@jesuits.org.zm Website: www.jctr.org.zm

Pa chifukwa chimeneci, Mfumu imene anapemphako thandizo ija inasandutsa Mfumu Ahazi kukhala m'modzi mwa akapolo ace komanso inamlamula kuti asiye kupembedza Mulungu wa Israeli. Pamene anazindikira kuti anapusitsidwa ndi Mfumu ina ija, Mfumu Ahazi anataya chiyembekezo ndipo anakana ndi kupemphera kwa Mulungu wa Israeli, Mulungu wa chipangano. Ngakhale mneneri Yesaya anayesako kumuuza Mfumu Ahazi ndi anthu onse kuti alimbe mtima chifukwa Mulungu wa mphamvu zonse ndiye mtetezi weni-weni wa Israeli, Mfumu Ahazi anakana ndithu kukhulupilira. Ndipo atakana ndithu kukhulupilira, mneneri Yesaya anayesa ndithu pompatsa chizindikiro Mfumu Ahazi chomuonetsa kuti akhulupilire Mulungu ndipo kuti azindikire kuti zomwe zili zosatheke ndi anthu zimatheka ndi Mulungu, chifukwa palibe kanthu kosatheka ndi Mulungu. Chizindikiro chimene anampatsa chinali chakuti virigo adzakhala ndi pakati naona mwana wa mwamuna amene adzamutce dzina loti Immanueli, kutanthauza kuti Mulungu ali nafe. Cholinga chake chinali chomuonetsa Mfumu Ahazi kuti anakakhulupilira Mulungu, Mulungu anakawapulumutsa anthu ake m'mabvuto aliwonse. Ahazi anakana ndithu ndi chizindikiro chimenechi ndipo zotsatira zake zinali zakuti iye pamodzi ndi ana a israeli onse anatengedwa ku ukapolo ku Babulo.

Tikawerenga Uthenga wa lero tikumva za munthu amene anali osiyana kwambiri ndi Mfumu Ahazi, mfumu yopanda chikhulupiliro. Uyu ndi Yosefe, munthu wachilungamo, wachikhulupiliro amene pomwe anakonzeka kutenga Virigo Maria kuti akhale mkazi wake anakumana ndi nkhani yobvuta kuimvetsa. Kodi zinatheka bwanji kuti Maria aononge chibewnzi chao ndi kukhulupilirana kwao potenga pathupi asanakhale pamodzi ngati banja? Yosefe sanakhulupilire ndi kumvetsa zimenezi. Koma posafuna kudziwonetsa munthu wolungama ndi kumchititsa manyazi Maria pomuulula poyera, malinga ndi momwe lamulo limanenera pa nkhani zoterozo, iye anaganiza zosamchita chipongwe Maria pomsiya ndi kumtumiza kwao msanga mwakachete-chete. Koma ngakhale zinali chonco, Yosefe anamkonda kwambiri Maria ndipo anali kumkhulupilira ndithu. Izi ndi zomwe anakakwanitsa kuchita pa ubwino wa umunthu wake, ngakhale anazindikira kuti zimenezi zinali zosakwanira ndithu. Nchifukwa chake Yosefe anakhalabe munthu wobvutika mumtima mwake ngakahale pamene anaganiza kuchita zimenezi chifukwa anali kumkhulupilirabe Maria. Nzoona Mulungu nthawi zonse amakhala okonzeka kutithandiza kufuna ndi kupeza njira zabwino mochotsera kapena mothetsera mabvuto ndi zinthu zomwe zimatisowetsa mtendere mu umoyo wathu. Pajatu achewa amati: "Chibale ndi pfupa, siciola." Mulungu ali nafe ndipo amakhala nafe nthawi zonse, pomwe tili ndi chimwemwe ndi mtendere komanso ndi pa mabvuto pomwe.

Chikhulupiliro chake Mfumu Ahazi sichinamthandize ngakhale pamene anampatsa chizindikiro kuchokera kwa mneneri Yesaya chomsonyeza kuti Mulungu angathe kupulumutsa anthu ake m'zobvuta zili zonse. Chkhulupiliro cha Yosefe ndicho chikhulupiliro cheni-cheni chifukwa ngakhale zinthu zinaoneka zosautsa ndi zobvuta kuzimvetsa mu umunthu wathu, pamene Mulungu anamuulira chinsinsi chake, Yosefe analeka kukaiaka natenga Maria kuti akhale mkazi wake. Iye anakhulupilira kuti zinthu zosatheka ndi anthu zimatheka ndi Mulungu. Motero Mulungu anakwanitsa kudzera mwa Amai Maria zomwe analonjeza kudzera mwa mneneri Yesaya kuti Mulungu kudzera mwa Yesu khristu anali kudzakhala nafe ngati munthu. Ndipo pokhala nafe ngati munthu, Mulungu amatipatsa mphamvu ife anthu kuti tilimbikire kufuna chilungamo ndi mtendere mngondya zonse za umoyo wathu.

Ndipo mneneri Yesaya mkulalika kwake, analosela za momwe ufumu wa Mulungu udzakhalire wa muyaya kusiyana ndi maulamuliro a pa dziko lino la pansi amene sakhalitsa. Nchifukwa chake Yesu anawazizwitsa alembi ndi aphunzitsi a malamulo amene anali kuyembekeza mesiya amene anakakhala mfumu yao yaulamuliro wapadziko lino la pansi. Monga Ahazi, mfumu yakale ija, alembi ndi aphunzitsi a malamulo naonso anakana kukhulupilira ndi kuzindikira kuti Yesu anali Immanueli, Mulungu ali nafe. Iwo anaona ndipo anamva kuphunzitsa kwa Yesu kwa ulamuliro ndi mphamvu komanso anaonanso mphamvu za Mulungu zimene zinali mwa Yesu makamaka pa machitidwe ndi pa milakuli yosiyana-siyana imene Yesu anachita. Mu zonsezi, Yesu anali kulalika ndi kumanga, mchikulupiliro, chiyembekezo ndi chikondi, ufumu awa Mulungu, ufumu wodzadza ndi chaulere, chilungamo, mtendere ndi chikondi. Tsono uyu ndiwo mutu wa uthenga wa tsiku la lero: "Musaope, Mulungu ali nafe." Ndi m'mene umoyo wathu ulili masiku ano m'dziko lino la Zambia, tikangodalira nzeru ndi mphamvu zathu kapenanso matalanta ndi mphatso zathu ndi kumaona kuti zonse tingathe

kukonza ndi kukwaniritsa pa ife tokha, sitidzapita msenga wautali. Tiyeni tidalire Mulungu, tikhulupilire kuti Mulungu alinafe m'mabvuto athu onse.

Kodi pakati pathu tingayambe motani kugawana zinthu zimene Mulungu anafuna kuti zikhale za onse, ndi kuthandizana pakati pa anthu ofooka ndi amene ali olimba, osauka ndi aja amene achitako bwino? Kodi tingakhale bwanji ndi ndale komanso ntchito za malonda/mabizimisi zomwe zilemekeza chilungamo ndi ubwino wokomera anthu onse nthawi zonse? Yankho ndiyoonekera poyera, monga inaonekeranso poyera munthu uja wachilungamo Yosefe; tiyenera kuzindikira kuti Mulungu ali nafe, mwa Yesu Khristu, Immanueli wobadwa mwa mzakazi wodzichepetsa Maria. Zomwe zinaoneka zosatheka, zinatheka ndi Mulungu. Izi ndi zoona ngakhale m'zinthu zomwe tikumana nazo m'dziko lino la Zambia masiku ano. Ndipo Yesu Mpulumutsi wathu wabwera ndipo akutiuza kuti "Ndine, musaope."

Mafunso Otithandiza Kusinkha-sinkha nd I Kugawana Mu Mabungwe/M'zimbumba

- Kodi ndi ciani cimene simatitayitsa chikhulupiliro pa nthawi za mabvuto m'mabanja athu, mumabungwe/m'zimbumba kapenanso m'dziko lathu la Zambia?
- Pokumana ndi mabvuto, Mfumu Ahazi analibe chikhulupiliro mwa Mulungu, pomwe Yosefe anali ndi chikhulupiliro mwa Mulungu. Kodi inu pomwe mukumana ndi mabvuto mumamkhulupilira ndithu Mulungu? Kodi kukhulupilira kwanuku mumakuonetsa motani?
- Kodi ndi phunziro lalikulu lotani lomwe mwaphunzira munyengo ino ya Adventi mchaka chino cha 2007 ndipo phunziroyo idzakuthandizani motani mchaka cha 2008?

Sewero

Pakhale munthu wamwamuna umodzi yemwe adzakhala Yosefe ndipo wina wamkazi yemwe adzakhala Maria. Yosefe azindikira kuti Maria ali ndi pakati ndipo asinkha-sinkha zomleka. Ali m'malingaliro amenewo, mnjelo wa Mulungu amuyendera namuonekera ndipo Yosefe akhulupilira kuti kudzera mwa Maria, lonjezo lomwe Mulungu anapanga kudzera mwa mneneri Yesaya Mulungu adzakwaniritsa. Ndipo Yosefe akondwera kwambiri.

Mapemphero a akhristu

- Tipempha Ambuye, kuti nthawi zonse tikhale anthu achikhulupiliro ndipo tikukhulupilireni ngakhale pomwe tikumana ndi mabvuto m'moyo wathu, m'mabanja athu mumabungwe/muzimbumba mwathu ndi m'dziko lathu. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutibvomereze.*
- Tipempha Ambuye, kuti tikhale ndi mtima wothandiza anzathu amene ali m'mabvuto osiyana-siyana ndi amene aponderezedwa. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutibvomereze.*
- Tipempha Ambuye, kuti tikulandireni ndi mtima wonse komanso ndi chimwemwe m'mitima ndi m'mabanja mwathu pomwe tichita Chaka cha Khrisimasi chaka chino. *Ambuye mutimvere, tikupemphani mutibvomereze.*